

UTHENGA WABWINO WA CHOONADI

Malangizo ndi Chilimbikitsa kuchokera m'Baibulo kupita kwa amene akulalikira Uthenga Wabwino

PALIBE MILUNGU INA KUPOSA INE

Anthu analengedwa ndi mzimu wamoyo. Kuyambira pachiyambi cha chilengedwe, anthu akhala akulakalaka kulambira chinachake. Pamene Yehova anafuna kukhala woyenera kumpembedza. Iye ndi yekhayo amene angakhutitse zosowa zauzimu za anthu zimene zili zakuya, koma anthu amapanga milungu yabodza ndi kudzipereka okha ku kutumikira mafano ogwirika ndi ziphunzitso zosagwirika. Uku ndiko kupembedza mafano, kumene kuli kudzipereka ku kulambira mafano, milungu yonyenga, kapena chilichonse chimene chimatenga malo a Mulungu Mwiniwake. Chilichonse chakuthupi kapena chauzimu kusiyapo Mulungu chomwe chimalamulira zokonda zathu, nthawi, mphamvu, ndalama ngakhale kudzipereka kwathu, chimenecho ndiye kupembedza mafano.


Pakhala pali mafano osema ndi milungu ya mitundu yosiyanasiyana ndipo yakhala ikutchedwa ndi maina osiyanasiyana mu zaka zochulukira zimene anthu akhala padziko pano. Chipangano Chakale nthawi zambiri chimanena za milungu yabodza ndi mafano a anthu achikunja. Dagoni, yemwe anali ndi mutu wa munthu ndi thupi la nsomba, anali mulungu wa Afilisti (1 Samuele 5:1-5). Merodaki kapena Beli, wa pa Yeremiya 50:2, anali “mbuye wa milungu ya kumwamba ndi dziko lapansi” ku Babiloni. Baala, mulungu wadzuwa, anali mulungu wamkulu wa Akanani. Malemba a pa 1 Mafumu 18 amanena za zimene zinachitikira Eliya ndi aneneri a Baala pamene amapemphera kuti moto ugwe kuchokera kumwamba. Pa 1 Mafumu 11:33, timawerenga za Asitoreti, mulungu wamkazi wa ubereki wa Asidoni; ndi Kemosi, mulungu wa Amoabu; ndi Milikommu, mulungu woombeza maula wa Aamoni. Mulungu wamoto, Moleki, amene kwa iye ana anali kuperekedwa

nsembe, alemba za iye pa Levitiko 18:21. Iyi ndi milungu yochepe chabe mwa milungu yopangidwa, zolengedwa zachinsinsi zomwe kawirikawiri zimafotokozedwa ndi makhalidwe a nyama ndi aumunthu, amene inachokera m'maganizo a munthu.

Malemba amafotokoza za chofooka chachikulu cha ana a Israele ku mibadwo yonse pamene ankatumikira Mulungu kenaka ndi kutembenukira ku mafano a dziko. Pa phiri la Sinai, Aisraele analamula Aroni kuti awapangire fano la mwanawang'ombe lagolide molingana ndi chifaniziro cha Aigupto amene ankapanga zifaniziro zoyenga ndi kumazilambira (Eksodo 32:1-4). Mose anatsika m'phirimo ndi lamulo la Mulungu, “Usakhale nayo milungu ina koma Ine ndekha. Usadzipangire iwe wekha fano losema, kapena chifaniziro chilichonse...Usazipembedzere izo, usazitumikire izo; chifukwa Ine Yehova Mulungu wako ndili Mulungu wansanje” (Eksodo 20:3-5). Lamulo la Mulungu limeneli ndi lofunika kwambiri ndipo lili ndi udindo kwa anthu onse kuti “musalambira mulungu wina” (Eksodo 34:14). Yesu anabwereza lamulo ili m'Chipangano Chatsopano: “Ambuye Mulungu wako uzimgwadira, ndipo Iye yekhayekha uzimtumikira” (Luka 4:8).

Mitundu yonse ya kupembedza mafano ndiponso kulambira ili tchimo kupatula kudzipereka komwe kumapita kwa Mulungu wa Kumwamba. Levitiko 26:1 amaletsa kupanga mafano ndi zipangizo zosema ndi kuzigwadira. Deuteronomo 4:15-19 amachenjeza anthu kuti asadziipitse ndi mafano. Amalangizidwa kuti asapange fano lofanana ndi nyama kapena anthu. Amachenjezedwa kuti asamalambire dzuwa, mwezi, kapena nyenyezi.

(Yapitirira pa tsamba 2)



“Usakhale nayo milungu ina koma Ine ndekha... pakuti Ine Yehova Mulungu wako ndine Mulungu wansanje.

Mau a Mkonzi

Phunziro la Baibulo:
Kupembedza mafano

Nkhani Yotsagana
nayo:
Kupembedza mafano
kwa dziko lapansi

Zizindikiro, Zithunzi,
Milungu, & Zochita

Kodi Mukudziwa?

Mau a Nyengo Yake

ZIMENE BAIBULO LIMAPHUNZITSA ZA...

Mau a Mulungu

2 Tim. 3:16-17; 2 Pet. 1:20-21; Mat. 24:35

Ubale wa Chikondi

Mat. 22:37-40; Yoh. 14:21-23; 1 Yoh. 4:7-11

Kulapa

Mach. 3:19; Mach. 17:30; 2 Akor. 7:10

Kubadwa mwatsopano

Yoh. 3:3-7; 2 Akor. 5:17; Aro. 6:1-4;
Aef. 2:1, 5-6

Kupulumuka ku uchimo

1 Yoh. 5:18; Mat. 1:21; Yoh. 8:11

Chidzalo cha Mzimu Woyera

Mach. 19:2; Mach. 15:8-9; Mach. 1:8

Chiyero

Luk. 1:73-75; Aheb. 12:14; 1 Pet. 1:15-16;
Tit. 2:11-12; Aro. 6:22

Ufumu wa Mulungu

Luk. 17:20-21; Aro. 14:17; Yoh. 18:36

Mpingo

Mach. 2:47; Aef. 4:4-6; 1 Akor. 12:12-13;
Akol. 1:18

Umodzi

Yoh. 17:20-23; Agal. 3:28; Chiv. 18:2-4

Maskaramenti

Mat. 28:19-20; Mat. 26:26-30;
1 Akor. 11:23-27; Yoh. 13:14-17

Machiritso

Luk. 4:18; Yes. 53:4-5; Yak. 5:13-16

Chiyero cha Banja

Mat. 19:5-6; Luk. 16:18; Aro. 7:2-3;
1 Akor. 7:10-11

Chikhalidwe cha pakati pa anthu ena

1 Tim. 2:9-10; 1 Akor. 11:14-15; Deut. 22:5

Masiku omaliza

2 Pet. 3:7-12; Yoh. 5:28-29; 2 Akor. 5:10;
Mat. 25:31-46

Kukhala mwa mtendere

Luk. 6:27-29; Luk. 18:20

Kupembedza

Yoh. 4:23-24; Aef. 5:19; 2 Akor. 3:17

Kulalikira Uthenga Wabwino

Mrk. 16:15

(Kuchokera pa tsamba 1)

Pali Mulungu woona mmodzi yekha, ndipo ulemu, matamando, ulemmero, ndi kudzipereka zonse nza Iye yekha. Yesu anatsogoza lamulo lalikulu koposa la kukonda choonadi ichi: “Mvera, Israele; Ambuye Mulungu wathu, Ambuye ndiye mmodzi” (Marko 12:29). “Popanda Ine palibenso Mulungu” (Yesaya 44:6). Milungu ina yonse iyenera kuthamangitsidwa, chifukwa kupembedza mafano a anthu kumalanda Mulungu kupembedza koyenera dzina lake.

Pakati pa mafano ndi zifaniziro za milungu pa Phiri la Mars, mtumwi Paulo akupereka uthenga wabwino wonena za Mulungu woona amene analenga kumwamba ndi dziko lapansi (Machitidwe 17:22-31). Mulungu sakhala m’nyumba zomangidwa ndi manja,



“Tisakhale ndi milungu
ina kuthupi kapena
m’mitima mwathu.”

ndipo sapembedzedwa ndi manja ao. Iye ndi Yemwe amapereka moyo ndi mpweya, ndipo Iye ndi Yemwe adzaweruza dziko patsiku loikika. Mulungu ameneyu sanapangidwe ndi golide, siliva, kapena mwala, ndipo sali chifaniziro cha zojambulajambula kapena chilengedwe cha munthu. Mulungu ameneyu ndiye mlengi wa chilengedwe chonse. Ali ndi mwana wamwamuna, Yesu, amene anapachikidwa ndipo anaukitsidwa kwa akufa m’masiku atatu. NDI MULUNGU

UYU yekha amene angabweretse mtendere wa moyo ndi kukwaniritsa chikhumbo chamkati cha moyo. Zoonadi, Mulungu ndi woyenera kutamandidwa, chifukwa zonse zinalengedwa kuti zimukondweretse (Chivumbulutso 4:10-11).

Zifanizo zonse za kupembedza, mafano onse olambiridwa, ndi zinthu zonse zolambiridwa ziyenera kuthetsedwa kotheratu m’miyoyo yathu. Mulungu ndi Mulungu wansanje (Eksodo 34:14), ndipo sangavomereze kusakaniza kupembedza mafano ndi kudzipereka kwa Iye. Pali mafano ndi milungu yabodza yambiri imene anthu amapempherabe kwa izo mpaka pano. Iyi ikhoza kutchedwa maina osiyana ndi a masiku akale, komabe iyo ikadali milungu yabodza ndi mafano. Maiko ambiri, mafuko, ndi maiko akupitirizabe kulambira mafano. Uku ndiko kupembedza mafano ndi kuchimwa.

Tisakhale ndi milungu ina kuthupi kapena m’mitima mwathu. Pamene anthu ena amakana mafano, ngakhale ambiri odzitcha Akhristu ali m’misampha ya kulambira kwachikunja ndi milungu yonyenga ya m’nthawi zakale. Tiyeni tiyeretse miyoyo yathu ndi kulambira kwathu kuti tikhale odzipereka ndi okondweretsa Mulungu mmodzi woona. ■

Gospel Truth ndi kalata imene imasindikizidwa miyezi itatu iliyonse ndi a mpingo wa Church of God pofuna kulangiza ndi kulimbikitsa kuchokera mu zoonadi zopezeka mu Baibulo. Kuti mudziwe zambiri werengani pa intaneti popita pa www.thegospeltruth.org ndipo muvomere pa email imene mulandire ngati mukufuna kuti mudzilandira nawo kalatayi. Kalata ya *Gospel Truth* imasindikizidwa mu maiko ambiri kuti iperekedwe kwaulere m’dzikomo ndipo chuma chothandizira ntchitoyi chimachokera ku ndalama zimene ena amapereka mwaufulu. Ngati mukufuna lisiti yoonetsa zimene mwapereka, tidzakupatsani. —Editor, Michael Smith

Gospel Truth, P.O. Box 2042, Nixa, MO 65714 USA
editor@thegospeltruth.org

Mau a Mkonzi



Ine ndine Yehova; dzina langa ndi lomweli; ndipo ulemerero wanga Ine sindidzapereka kwa wina, ngakhale kunditamanda kwa mafano osemmedwa. — Yesaya 42:8

Mulungu ndi waulemerero ndipo ntchito zake ndi zodabwitsa. Palibe chinthu china chilichonse kumwamba kapena padziko lapansi chimene chingayambepo pa kufanizira ndi ukulu ndi mphamvu za Yehova Mulungu. Iye akuyenera ulemu ndi ulemerero ndipo sadzapereka matamando ndi ulemu umenewo kwa chinthu china chilichonse kapena fano loseema. Ndi Mulungu yekha amene angaombole anthu, ndipo ndi Mulungu yekha amene ali ndi mphatso ya moyo wosatha yakuti apereke.

Nkhani yathu ulendo uno ili pa mutu wa kupembedza mafano. M'dzikoli muli zipembedzo zambiri zimene anthu amagwadira ndi kupembedza mafano. Palinso anthu ambiri amene akulambira mafano amene sanasemedwe ndi miyala kapena kupangidwa ndi wosula zitsulo. Anthu akudzipereka ku zinthu za m'dzikoli, ndipo ngakhale kuti anthu ambiri safuna kuvomereza, kumeneko ndiko kupembedza mafano.

Akunja ndi opembedza mafano akuyenera kusiya milungu yao yabodza ndi kutsatira Mulungu mmodzi woona. Nyumba zao ziyenera kuchotsedwa mafano ndi zizindikiro zonse za kupembedza mafano, ndipo Mau a Mulungu ayenera kukhala oyamba m'mitima yao. Akhristu ambiri angavomereze zimenezi, koma nanga za milungu ina? Kodi nanga za mulungu wa zokonda chuma ndi wokonda dziko? Kodi nanga za mulungu wodzikonda? Kodi nanga za fano la ziphunzitsa za mpingo ndi fano la abusa ndi aneneri? Kodi ife monga Akhristu tingazindikirenso zimenezi monga ngati machitachita olambira mafano?

Kodi nanga timaononga nthawi yathu motani? Kodi ndi zotheka kuti mchezo wa pa intaneti kapena masewero akhale mafano kwa ife? Awa amakhala mafano ngati tiwalola kuti azilambulira nthawi yathu ndipo kuti miyoyo yathu idzitsogozedwa ndi zimenezi. Ngati tidzipereka kwambiri kwa mafanowo kuposa kulambira Mulungu, kodi kumeneko sikulambira mafano? Ndi zodabwitsa kuti anthu atha kuononga ndalama ndi nthawi pa zinthu za m'dzikoli mosavuta, koma pankhani ya utumiki wa Yehova, sipakhala ndalama zokwanira kapena nthawi yokwanira. Kodi zimenezi siziyenera kusowetsa mtendere mzimu wathu?

Zimatengera kudziunguza ndi kukhala oona mtima kwambiri kuti munthu avomereze kuti pakhoza kukhala zinthu zina m'moyo wake zimene akuziyikira kumtima mwanjira njira yakuti zikulanda ulemerero woyenera kupita kwa Mulungu ndiponso malo ake apamwamba amene Iye yekha ayenera kukhala nao. Timaona zinthu kuchokera ku mapenyedwe apafupi, komanso aumbombo mokhudzana ndi zinthu zathupi. Ambuye atithandize kuti tibwerere pambuyo ku moyo uno ndi machitidwe athu ndikudzifunsa kuti: “Kodi Mulungu amaziona bwanji?” Kodi tikutumiza uthenga wotani kwa Mlengi wathu ngati tidzilowetsa m'machitidwe olambira mafano kapena kugwirizana ndi khamu la olambira mafano m'maphwando ao, amene nthawi zonse amanena kuti, “Mtima wanga uli wolungama.”

Ukwati, tikawuyerekeza ndi ubale ndi Mulungu, umayenera kukhala ubale wokhazikika. Kodi ndi uthenga wanji umene ndingakhale ndikupereka kwa mkazi nditakhala kuti ndikadasungabe pa desiki panga chithunzi cha bwenzi langa lakale ndi kumakumbukira tsiku lake lobadwa chaka chilichonse? Kodi pangakhale kusiyana nditamuuza mkazi wanga kuti sizinali mu mtima mwanga? Kodi izi ndi zosiyana ndi Mulungu? Ambuye, tithandizeni kuti tichotse kupembedza mafano konse ndipo tikonde Mulungu ndi mitima yathu yonse.

Michael W. Smith

January 2023



Mukafuna kutipeza

pa intaneti, mulembe

www.thegospeltruth.org

kuti mudzilandira makalata

athu kapenanso kuti

muone makalata akale.

Kodi Mulungu ndi woyamba? Zindikirani mafano amakono

Zokonda zanga zili kuti? Zokhumba zanga zili kuti? Maganizo anga amakutidwa ndi ziti? Nthawi yanga imathera kuti? Ndalama zanga ndimazigwiritsa kuti?	Ndalama/Zinthu zakuthupi Ntchito/Kudziwika Chikoka/Kutchuka Maonekedwe athupi Masewero/Zosangalatsa	Maubale Osaopa Mulungu Mafoni/Tekinoloje Ziphunzitsa Zachipembedzo Maphunziro Zokhudza dziko
---	--	---



Kalozera powerenga Baibulo

Mutu: Kulambira mafano

Kuwerenga Malemba: Ambuye Mulungu wako uzimgwadira, ndipo Iye yekhayekha uzimtumikira. — Luka 4:8

Tanthauzo: Kupembedza mafano kumatanthauzidwa kukhala “kulambira mafano, mafano, kapena chilichonse chimene chisali Mulungu; kulambira milungu yonyenga. Kukonda kwambiri, kapena kulemekeza chilichonse; ulemu kapena chikondi chimene chimalekezera kupembedza” (Merriam-Webster Dictionary).

Mwachidule: Kukweza ndi kupembedza china chilichonse kusiyapo Mulungu Mwiniwake ndiko kupembedza mafano—kaya ndi fano, mulungu wopangidwa, zipembedzo za munthu, kapena china cha dziko lapansi chimene chimalamulira chikondi, nthawi, mphamvu, ndi ndalama.

I. Pali Mulungu mmodzi

- A. Marko 12:28-29 Yehova Mulungu wathu ndi Ambuye mmodzi.
- B. Yesaya 44:6 Palibenso Mulungu kupatula ine.
- C. 1 Timoteo 2:5 Mulungu mmodzi ndi mkhalapakati mmodzi.
- D. Chivumbulutsa 4:10-11 Yehova ndi woyenera kupembedzedwa.

II. Kupembedza mafano kukukanizidwa

- A. Eksodo 20:3-5 Musakhale ndi milungu ina, musapange fano losema; Ambuye ndi wansanje.
- B. Deuteronomo 4:15-19 Musapembedze mafano, dzuwa, mwezi, kapena nyenyezi.
- C. Levitiko 26:1 Musapange mafano.
- D. Deuteronomo 7:3-4 Musakwatire opembedza mafano.

III. Lambirani Mulungu yekha

- A. Luka 4:7-8 Lambirani Yehova yekha.
- B. Mateyu 6:24 Palibe munthu angathe kutumikira ambuye awiri.

IV. Mulungu wona komanso mafano

- A. Machitidwe 17:22-31 Mulungu ndi Mlengi, osati wolengedwa.
- B. Deuteronomo 4:28 Ntchito ya manja a anthu.

V. Kupembedza mafano mu Chipangano Chakale

- A. Fano la Mwanawang’ombe: Woimira wa Yehova kapena chinthu cholambiridwa cha Aigupto (Eksodo 32:1-4).
- B. Fano la golide la Nebukadinezara (Daniele 3:1-5).
- C. Dagoni: Mulungu wa Afilisti; mutu wa munthu ndi thupi la nsomba (1 Samuele 5:1-5).
- D. Merodaki (Marduk, Bel): Mbuye wa Babulo wa milungu yakumwamba ndi dziko lapansi (Yeremiya 50:2).
- E. Baala: mulungu wamkulu wa Akanani—mulungu wadzuwa, namondwe, mulungu wobala (1 Mafumu 18:21-40).
- F. Asitoreti: mulungu wamkazi wa ku Sidoni wa kubala ndi ubereki.

- G. Kemosi: mulungu wa fuko la Amoabu; nsembe yaumunthu.
- H. Milkomu: mulungu woombeza wa Aamoni (1 Mafumu 11:33).
- I. Moleki: mulungu wamoto, kupereka nsembe za ana (Levitiko 18:21).

VI. Mulungu wa dziko lino

- A. 2 Akorinto 4:4 Mulungu wa dziko lapansi achititsa khungu maganizo.
- B. Aefeso 2:2 Mkulu wa mphamvu ya mlengalenga.
- C. Aefeso 6:10-13 Mphamvu ndi olamulira amdima.

VII. Kulambira kwa chipembedzo chonyenga ndi mwambo

- A. Chivumbulutsa 14:8-10 Chilombo ndi fano lake.
- B. Marko 7:6-9 Kukweza miyambo ya anthu.

VIII. Kupembedza kwa anthu

- A. Machitidwe 12:21-23 Herode anakalambiridwa ngati mulungu.
- B. 2 Atesalonika 2:3-4 Munthu wauchimo.
- C. Machitidwe 14:12-15 Paulo ndi Baranaba anakana kupembedzedwa.
- D. Chivumbulutsa 19:10 Musapembedze wamthenga.
- E. Yohane 7:16-18 Kudzikweza kosiyana ndi Khristu.
- F. 2 Akorinto 4:5 Musadzilalikire nokha.

IX. Kulambira mafano a Chipangano Chatsopano

- A. Akolose 3:5 Kusirira kwa nsanje ndiko kupembedza mafano.
- B. Afilipi 3:19 Mulungu wao ndiye mimba zao.
- C. Aroma 16:18 Kudzitumikira wekha osati Yesu.

X. Kulambira zinthu za dzikoli

- A. 1 Yohane 2:15-16 Musakonde zinthu za dziko lapansi.
- B. Aroma 1:23-27 Chilengedwe; kugonana kwa amuna kapena akazi okhaokha.
- C. 1 Timoteyo 6:10-11 Kukonda ndalama.
- D. 2 Timoteo 2:3-4 Zinthu za moyo uno.

XI. Chiweruzo chotsutsa kulambira mafano

- A. Agalatiya 5:19-21 Opembedza mafano sadzalowa mu ufumu wa Mulungu.

KUPEMBEDZA MAFANO KWA DZIKO LAPANSI

Munthu safunikira kuti ayang'ane ku zitukuko zamasiku akalekale kuti apeze kupembedza mafano ndi milungu yonyenga. Pali mafano ponse potizungulira ife masiku ano.

Kupembedza mafano kuli koposa kungogwadira fano ndi kulilambira. Kupembedza mafano ndi chilichonse chimene munthu amachikonda ndipo amadziperereka kwa icho kuposa Mulungu. John Calvin analondola pamene analemba kuti: "Mtima wa munthu uli ngati fakitale imene nthawi zonse imapanga mafano."



**"Chinthu chikakhala
chamtengo wapatali
kuposa Mulungu
ndi Mau ake
ndipo chinthucho
nchodalirika
kuti chibweretse
chikhutiro,
chimasanduka fano."**

Kulambira mafano kwa masiku athu

Mosiyana ndi malamulo a Mulungu, masiku ano zilipobe zipembedzo zambiri zimene anthu amagwadira mafano osema achitsulo kapena amiyala. Komabe, pamene gawo lalikulu la dzikoli lakana mafano amenewa, pali mafano ena okulirapo ndi amphamvu kwambiri a mu mtima ndi m'aganizo amene aimikidwapo amene anthu akutayirapo nthawi, ndalama, ndi chikondi. Chilichonse chomwe timachiikira kumtima kapena kuchitenga kukhala chofunikira m'moyo uno kuposa Mulungu chimakhala fano. Thunthu lenileni la kupembedza mafano lili mu mtima ndipo limapezeka mu zimene munthu amakonda, kuzikhulupirira, ndi kuzilambira.

Nkhondo yauzimu

Tili pankhondo yauzimu yolimbana ndi Satana pamodzi ndi mizimu yake yonyenga amene akuyesetsa kutibera mitima yathu kusiya kulambira koono kwa Mulungu. "Chifukwa kuti kulimbana kwathu sitilimbana nao mwazi ndi thupi, komatu nao maukulu, ndi maulamuliro, ndi akuchita zolimbika a dziko lapansi a mdima uno, ndi auzimu a choipa m'zakumwamba" (Aefeso 6:12).

Mphamvu zoipa zili ponseponse, zikusonkhezera anthu kulambira pa guwa la nsembe la kudzikonda, zosangalatsa, masewera, chipembedzo, ndale, zadziko, zasayansi, maphunziro, ndi kukonda chuma. "mulungu wa nthawi ino ya pansu pano anachititsa khungu maganizo ao a osakhulupirira" (2 Akorinto 4:4).

Kulambira mafano m'chipembedzo

Kupembedza mafano kumapezeka osati m'chikunja chokha komanso m'Chikatolika ndi Chiprotestanti. Mpingo wa Chikatolika ndi odzaza ndi miyambo yachikunja ndi miyambo yomwe ilibe maziko mu Mau a Mulungu amene ali angwiro. Kukwezedwa kwa chipembedzo cha mtundu uliwonse ndiwo mtundu wina wa kupembedza mafano. "Ngati wina alambira chilombocho [Chikatolika], ndi fano lake [Chiprotestanti], nalandira lemba pamphumi pake, kapena padzanja

lake iyenso adzamwako kuvinyo wa mkwiyo wa Mulungu" (Chivumbulutso 14:9-10). Nthawi zambiri anthu amadziperereka ku cholinga cha chiyanjano chao kapena gulu lachipembedzo kuposa ntchito ya Khristu Mwiniwake. Uku ndi kupembedza mafano. Pa Marko 7:6-9, Yesu analankhula za anthu amene amamulemekeza Iye ndi milomo yao, koma mitima yao inali kutali ndi Iye. "Musiya lamulo la Mulungu, nimusunga mwambo wa anthu." Ngakhale anthu anene kuti amakonda Mulungu, kuli kulambira mafano ngati iwo amakweza miyambo yao kuposa chopusa cha Mau a Mulungu. Izi zikhoza kukhala zoono kwa oyera mtima a Mpingo wa Church of God. Kukhulupirika ndi kudzipereka ku mwambo kapena chiphunzitso (ngakhale zikhale zolondola motani) zimenezi zikhoza kusanduka kulambira mafano pamene zapatsidwa malo akuti zikhazikike koipitsitsa m'moyo wa munthu kapena mpingo.

Kupembedza munthu

Kukweza atsogoleri andale ndi achipembedzo ndi kuwapatsa ulamuliro ndi kudzipereka koyenera kwa Mulungu yekha kulinso mtundu wa kupembedza mafano. Pa Machitidwe 12:21-23, Herode anakamba nkhani yaikulu kwa anthu. Iwo anafuula kuti: "Ndiwo mau a Mulungu, si a munthu ai." Ndipo pomwepo mngelo wa Ambuye anamukantha Herode ndipo anadyedwa ndi mphutsi chifukwa "sanampatse Mulungu ulemmerero." 2 Atesalonika 2:3-4 amachenjeza za kunyengedwa, popeza munthu wauchimo adzadzikweza yekha pamwamba pa Mulungu ndi kulambiridwa monga Mulungu. Lembali kawirikawiri limagwirizana ndi papa wachikatolika amene amadzinenera kukhala wolowa m'malo mwa Khristu padziko lino lapansi. Kumeneku ndiko kuchitira mwano Mulungu komanso kupembedza mafano. Komabe, pali 'apapa aang'ono' ambiri amene amakhala monga oyang'anira, abusa, ndi atsogoleri m'mipingo ndi mabungwe achipembedzo. Amadziyika okha pamlingo wokwezeka ndipo kuti mau ao ayenera kuganiziridwa pamlingo wa malemba. Anthu akhoza kuwanthunthumirira mwamantha ndi kufuula ndi kulengeza kuti ali nga nga nga pambuyo pao mu zauzimu pokhala amuna ndi akazi a Mulungu, komatu uku ndiko kupembedza mafano ndithu.

(Yapitirira pa tsamba 6)

Khristu ndiye woyenera kutamandidwa, osati munthu. Paulo ndi Baranaba anachita zozizwitsa mpaka anthu anayamba kuwaona ngati milungu imene inabwera pakati pa anthu (Machitidwe 14:12-15). Amuna oona a Mulungu awa anakana kutamandidwa ndi kulambiridwa ndipo analengeza kuti iwo anali “anthu a mkhalidwe wathu umodzimidzi wanu.” Yohane amene analemba buku la Chivumbulutso anagwada pansi nalambira mngelo amene anaona masomphenya. Mngeloyo anayankha kuti: “Tapenya, usatero; ine ndine kapolo mnzako, ndi mnzao wa abale ako akukhala nao umboni wa Yesu; lambira Mulungu” (Chivumbulutso 19:10). Anthu alionse amene amalambira atsogoleri ao auzimu ali ndi mlandu wa kupembedza mafano, chimodzimidzinsu atumiki a Mulungu amene amavomereza kutamandidwa ndi kupembedzedwa kotereku.

Kudzipembedza wekha

Kudzitikumula kwamtundu uliwonse kungakhale kupembedza mafano. Kudzipembedza ndi chimodzi mwa mafano akuluakulu mu m'badwo uno. Izi zikukhudza zinthu zauzimu komanso za dziko. Yesu ananena kuti, “Iye wolankhula zochokera kwa iye yekha afuna ulemu wa mwini yekha” (Yohane 7:16-18). Iye ananena za iye yekha. Mu magulu achipembedzo, atumiki a Mulungu ochuluka kwambiri amalankhula za iwo eni ndi kukweza njira zao, pamene mtumwi Paulo ananena kuti: “Pakuti tilalikira si za ife tokha, koma Yesu Khristu Ambuye” (2 Akorinto 4:5). M'mau achipembedzo, alaliki ambiri amalankhula za iwo eni ndi kukweza njira zao. Tikukhala mu nyengo imene anthu amadalira maganizo ao, malingaliro ao komanso njira zao. Amangoganizira za iwo okha ndipo amakhala moyo wodzikonda ndi wodzikundikira. Uku ndi kupembedza mafano kumene sikusiyana ndi kugwadira fano lochita kusema.

Pa Afilipi 3:19 amanena za anthu amene “mulungu wao ndiye mimba yao, ulemerero wao uli m'manyazi ao, amene alingirira za padziko.” Anthu akukana zinthu zopatulika za Mulungu ndipo akudzipereka okha ku zokondweretsa ndi zokhutiritsa zao. Iwo amalambuliridwa ndi ‘mimba yao’ ndipo amachita zinthu zimene amaona kuti nzosangalatsa thupi. Iwo “satumikira Ambuye wathu Yesu Khristu, koma mimba yao” (Aroma 16:18). Izi sizimakhudza kususuka pa zakudya kokha komanso zinthu zonse zathupi zomwe zimalumulira anthu.

Milungu ya dziko lino

Mulungu ali woyenera kuti tizimukonda, koma ambiri akupereka zokonda zao ku zinthu za m'dzikoli. “Musakonde dziko lapansi, kapena za m'dziko” (1 Yohane 2:15). Chilakolako cha thupi, chilakolako cha maso, ndi masiriro a moyo, zakhazikika pa mafano amakono. Kodi anthu amasirira ndi kulambira chiyani? Kodi nchiyani chimawadyera nthawi, ndalama komanso mphamvu zao? Kodi anthu amalemekeza chiyani ndikutembenukira kuti mu nthawi yao yakusowa? Kodi kukondweretsa thupi, zotukula dziko lao, mafashoni, masewera, ndi zosangulutsa sizigwirizana ndi kakhaliidwe kameneka? Zinthu zovomerezeka zimatha kukhala mafano. Anthu ambiri akupereka nsembe zao pa maguwa a mafano amakono amenewa.

Kuchokera kulambira mafano kufikira ku chikhalidwe cholakwika

Lemba la Aroma 1:23-27 limafotokoza mmene anthu anasinthira ulemerero wa Mulungu nkukhala chifaniziro cha munthu, mbalame, ndi nyama. Vesi 26 limanena kuti iwo ‘anatumikira cholengedwa ndi kusiya Wolengayo’. Izi zikuchitika m'njira zambiri, koma lembalo likunena mwachindunji kuti kupembedza kumeneku ndi kwa cholengedwa kumene kukukhudzana ndi chilakolako ndi machitidwe a kugonana kwa amuna kapena akazi okhaokha. Ngakhale kuti pakati pathu izizi zafala ndipo zikutengedwa ndi ambiri kukhala zovomerezeka komabe ena sakuzivomera, umenewu ndi uchimo ndi gawo limodzi la kupembedza mafano kopyolera muyeso.

Kulambira “Zinthu”

Akolose 3:5 amatiphunzitsa kuti kusirira kwa nsanje ndiko kupembedza mafano. Kukonda zinthu zakuthupi, chuma, kutchuka, mphamvu, ndi kutchuka ndiko kupembedza mafano chifukwa kumaononga chimene chiyenera kukhala cholinga chachikulu ndi chotipangitsa kuti tilambire ndi kutumikira Mulungu. “Pakuti muzu wa zoipa zonse ndiwo chikondi cha pa ndalama” (1 Timoteo 6:10). Ambiri anasokera pa chikhulupiriro pamene adayamba kutsatira ndi kutumikira zinthu za dziko lapansi koposa Mulungu mwini. Kodi nchiyani chikulumulira nthawi yanu, ndalama zanu, ndi mphamvu zanu? Kodi mumaika Mulungu ndi ntchito zake patsogolo kuposa zinthu zina? Kodi mumapatula nthawi yotumikira mokhulupirika ndi oyera mtima kapena mumadzikhululukira nokha pamene mukudzipereka kuzinthu zina? Mitima imaululidwa ndi zisankho komanso zimene timazisankha mu moyo. Kodi nchiyani chimalumulira kumene mukukhala, amene mudzakwatirane naye, zimene mumachita, ndi kumene mukupita? Kodi ndizotheka kuti mwina fano latenga malo a Mulungu m'moyo wanu?

Kukwezedwa kwa zinthu zabwino

Paulo anachenjeza Timoteo kuti: “Msilikali sakodwa nazo ntchito wamba” (2 Timoteo 2:3-4). Mu nthawi yathu ino, pali zinthu zooneka kuti tikuyenera kukhudzika nazo ndi kuthandizapo, komabe sitikuyenera kutanganidwa nazo. Pali zochitika zandale, zamakhaliidwe, zamitundu ya anthu, ndi zachikhalidwe cha anthu zimene zikhoza kukopa munthu msangamsanga mpaka kufika pamlingo umene zikulumulira ndi kukhala fano lake. Inu mwana wa Mulungu, chenjerani kuti musakodwe nao muzinthu zomwe zingaoneke ngati ndi zabwino. Posachedwapa, zabwino zija zimadzakhala zofunika kwambiri kuposa Mulungu komanso njira yake yachikondi, chikhululukiro, ndi kuleza mtima.

Lambirani Mulungu Yekha

Mafano amasiku ano ndi achinyengo komanso oopsa kwambiri kuposa mafano agolide ndi siliva. Pali Mulungu mmodzi, ndipo chikondi chathu ndi utumiki wathu kwa Iye zikuyenera kupita kwa Iye basi. Tiyeni tidziyese tokha kuti tione ngati pali mafano amene ayenera kugwetsedwa. Chotsani ndi kudziyereza nokha ku mafano a dziko lapansi, pakuti zoonadi, opembedza mafano ndi “iwo akuchitachita zotere sadzalowa Ufumu wa Mulungu” (Agalatiya 5:19-21). ■

Zizindikiro, Zithunzi, Milungu ndi Miyambo

KUZIKIKA MU KUPEMBEDZA MAFANO



Chithumwa: Chinthu chomwe chimaonedwa kuti chili ndi mphamvu zachipembedzo kapena zamatsenga pofuna kuteteza, kuchiritisa, kapena kuvulaza anthu (chitsanzo ~ mtanda, zotsutsana, phazi la kalulu, mikanda, timiyala tamtengo wapatali).

Mai Maria: Maria, amai a Yesu, amene Akatolika anayamba kupemphera kwa iye m'zaka za ma 400AD.



Buddha: 'Woukitsidwa' kapena 'Wowunikiridwa' wochokera ku South Asia m'zaka za mma 600AD. Ngakhale kuti satengedwa kukhala mulungu, anthu a chi buddha amagwadira fano lake mwaulemu ndi kufunafuna kupeza mphamvu zabwino zauzimu.

Ganesh: Imodzi mwa milungu yachihindu yodziwika bwino komanso yolambiridwa. Mbuye wachipambano ndi wochotsa zopinga.



New Age: Zinthu zonse ndi chimodzi. Gulu la zikhulupiriro zosiyanasiyana zauzimu zomwe zimafuna mgwirizano mwachilengedwe komanso mwa mwini yekha. Mulungu ali mu chilichonse ndipo munthu ndiye mulungu. Malingaliro amalenga zenizeni. Zochita zao zambiri zimakhala zamatsenga.

Kupembedza mizimu yamakolo: M'madera ena makolo amene anapita amalemekezedwa monga mizimu, ndipo amakhulupirira kuti akhoza kuchenjeza, kuteteza, ndi kutsogolera moyo watsiku ndi tsiku. Nthawi zina amapemphera kwa mizimuyi ndipo amayisiira chakudya kuti idye.



Ufiti: Kugwiritsa ntchito mphamvu kapena matsenga pofuna kulumulira anthu kapena zochitika.

Nyenyezi: Mtundu wa maula amene amalosera zimene zidzachitike poona maiko ena amene ali kumwambaku komanso nyenyezi. (zizindikiro za nyenyezi).



Matchuthi

Pamene pali njira zololezeka mwauzimu za kusangalala ndi maholide ena adziko, mwana wa Mulungu sakuyenera kumawasunga nthawi zonse. Momwemonso dziko lapansi. "Chilichonse chimene muchita, chitani ku ulemerero wa Mulungu." – 1 Akorinto 10:31



Easter (Sitiyenera kusokonezedwa ndi Lamulungu la Kuuka kwa Khristu): Kawirikawiri chimatengedwa kuti chinali tchuthi chachikunja chokondwerera mulungu wamkazi wa masika ndi kubala. Kalulu anali chizindikiro cha kubala ku Iguputo wakale, motero pamakhala kalulu pa Easter. Mazira anali chizindikiro cha kubala ndi moyo ndipo kupaka mazira mitundu yosiyanasiyana kunayambira kalekale pa miyambo yachikunja imeneyi.



Halowini: Poyamba inali tchuthi yachikunja yokondwerera Samhain. Chiyambi cha nyengo yachisanu ya Celtic; nthawi yolemekeza akufa pamene malire pakati pa amoyo ndi akufa adachepa. Maungu osemmedwa ankagwiritsidwa ntchito pofuna kuthamangitsa mizimu yoipa. M'zaka za ma 900AD, mpingo wa chiKatolika unayesa kuchotsa chikondwerero ichi cha a Celtic ndipo m'malo mwake unaika Tsiku la Oyera Mtima Onse.



Khristimasi: Poyambirira inali tchuthi yachikunja pamene anakondwerera nyengo yachisanu ndi kubadwanso kwa mulungu wa dzuwa. Mpingo wa chiKatolika unatenga tsiku la tchuthilo ndi "kulipangitsa kukhala lachikhristu" koterokuti anthu achikunja otembenuzidwa kuti apitirize ndi chikondwerero chokhala ngati chomwecho. Kugwiritsidwa ntchito kwa nkhatu ndi mitengo yobiriwira chinali chikhalidwe chimene chimachitika pazipembedzo zachikunja.



Chiyambi cha Steeples: Mbiri ya nsanja yaitali inayambira zaka masauzande ambiri kuchokera ku kulambira kwachikunja kwa Aigupto. Chinali chizindikiro cha nsanja yaitali ndi yosongoka chomwe chinkalemekeza mulungu wa dzuwa ndi ubereki. Zizindikiro zambiri zachikunja zinaphatikizidwa ndi mpingo wa chiKatolika m'zaka za ma 500AD. Nsanjayo inkagwiritsidwa ntchito ngati malo oonera patali, kuti mabelu amveke kutali,



kuthamangitsa mizimu yoipa, komanso kutanthauza kufika kumwamba. Inakhala gawo la kamangidwe ka matchalitchi ndipo inasonyeza kuti nyumbayo ndi malo olambiriramo.



KWA IYE KUKHALE ULEMERERO


Koma kulani m'chisomo ndi chizindikiritso cha Ambuye wathu ndi Mpulumutsi Yesu Khristu; kwa Iye kukhale ulemerero, tsopano ndi nthawi zonse. Amen. — 2 Petro 3:18

Kuti Mutipeze

The Gospel Truth
P. O. Box 2042
Nixa, MO 65714
USA

Email:
editor@thegospeltruth.org

Ziboliboli ndi zipilala zizamangidwa kuti zikumbukire akufa ndi kulimbikitsa amoyo; ma yunivesite akuluakulu amamangidwa kuti apititse patsogolo chidziwitso cha anthu ndikulemekeza luntha la munthu; nyumba zitalizitali zikhoza kuchitira umboni nzeru ndi luso; ndipo nyumba zosungira ndi kuwerengera mabuku ogwirika komanso apakompyuta zili zodzaza ndi nzeru za anthu. Iwe mwana wa Mulungu, kodi ndi mfundo iti ya dzikoli imene tidzayesetse kutsogozedwa nayo? Kodi tidzalemekeza ndi kukweza ndani ndi moyo wathu?



Mfundo yeniyeni komanso cholinga cha ana a Mulungu tsiku ndi tsiku chidzikhala chofuna kulemekeza Yesu Khristu monga Ambuye ndi Mpulumutsi wa dziko lapansi. Pomwe anthu adziko lapansi amadzikweza mu zomwe adachita ndikukonzekera kuchita, kukwezedwa kwathu kuyenera kukhala mwa Khristu yekha.

CHIYERO CHA KWA AMBUYE

Tiyeni tifunefune kudziwa ndi kumvetsetsa Khristu kuti tikule mu chisomo chake cha umulungu mwa chikoka ndi mphamvu ya Mzimu wa Mulungu. Pamene tikonda ndi kumvera Mulungu, kugonjera kwathu ndi kudzikhuthula kwathu kudzachuluka, ndipo tidzakhala ndi khalidwe longi la Khristu mwini. Mwakutero, ndi Khristu yekha amene adzakwezedwa. Mfundo iliyonse, zolinga, zimene tikuyesayesa, maloto, ndi zokhumba zilizonse zikhazikike pa maziko a Khristu, ndipo nthawi zonse tifunefune ulemerero wa mpulumutsi mmodzi yekha wa dziko lapansi.

Ulemu wonse, ulemerero ndi chiyamiko zonse zikhale za Yesu Khristu, pakuti Iye ndiye Mbuye wa ambuye, Mfumu ya mafumu, Alefa ndi Omega, chiyambi ndi mapeto, woyamba ndi wotsiriza wa chikhulupiriro chathu. Iye ali ndi mphamvu zonse ndi ulamuliro ndipo amalamulira pa milungu iliyense ndi mizimu yapadziko lapansi.

Tikhoza, tingathe, ndipo tiyenera—popanda kupepesa ndi popanda kuchita manyazi—kukhala ndi moyo wolemekeza Ambuye Yesu mphindi iliyonse, mpaka muyaya, kumene tidzakhala kosatha pamaso podabwitsa pa Mulungu Wamphamvuyonse. Iye ndi woyenera kutamandidwa ndi kumulambira mu chochitika chilichonse cha moyo uno. Kwa Iye kukhale ulemerero m'nthawi ya mayesero, m'moto, mumdimu, m'misozi, ngakhale mu imfa. Si chinthu chovuta koma ndi chaulemu kulemekeza Ambuye wathu. ■